

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Malangizo ndi Chilimbikitsa
kuchokera m'Baibulo kupita kwa
amene akulalikira Uthenga Wabwino

MULUNGU NDIYE KOTHAWIRA KWATHU

Mulungu ndiye pothawirapo pathu ndi mphamvu yathu, thandizo lopezekeratu m'masautso.

—Masalimo 46:1

Kodi ndi chifukwa chiyani tikuyenera kukhala ndi pothawirapo? Kodi ndiye kuti chipulumutso kudzera mwa Khristu sichipangitsa kuti ana a Mulungu asakumane ndi mavuto, zowawa, ndi zisoni za moyo uno? Yankho lake lomvekeratu ndi lakuti “Ayi.” Chipulumutso ndi chinthu chochitika modabwitsa komwe kuli kuombedwa ku uchimo ndi kukanidwa. Pali mtendere wamumtima, chimwemwe mwa Mzimu Woyera ndiponso chiyembekezo cha moyo wosatha. Komabe, chifukwa chakuti timakhala mu dziko lauchimo ndipo ndife zolengedwa ndiponso timakhudzidwa ndi zimene zimachitikira matupi ndi maganizo athu, tonsefe timakumana ndi zovuta. Zilipo nthawi zimene dzuwa limaoneka kuti silikuwala, ndipo zisoni za moyo, zakunja ndi zamkati zomwe zidzayesera kuzungulira miyoyo yathu. Pamene mtima wazingidwa ndi katundu wochulukira, zoonadi zake nzakuti pamene pakufunira thandizo lothawirapo.


Tiyamika Mulungu kuti pali thandizo kumene tikhoza kuthawirako m'nthawi ya msautso. Masalimo 46 ndi ndime ya chithonhozo ndipo imatumikira ku mtima wosweka komanso ku moyo umene uli pa chiopsezo chakuti ukhoza kumira mu mavuto a moyo uno. Mau akuti kothawirapo akukamba za malo obisilirako, malo amene ukhoza kuwadalira ndiponso malo amene unghathawireko kuti ukhale otetedwa. Ngakhale kuti aliyense m'moyo uno amakhala ndi mavuto, ndipo ambirinso amafuna popumulira, chithonhozo kapenanso kupulumuka ku zinthu za dziko lino, palibe chimene tingachifanizire ndi thandizo limene likupezeka mwa Mulungu yekha. Ndi kwa Iye kumene tikuyenera kuthawirako munthawi zimene tikusowa pogwira ndinso pamene tili m'mavuto. Iye yekha ndi amene akhoza kupereka malo a chitetezo ndi chithonhozo

ndipo adzatumikira ku zopweteka zozama zimene anthu ambiri amakumana nazo.

Oyera mtima a Mulungu ochuluka adutsa mu nyengo zosautsa; ena mavutowo anangowasunga mumtima ndipo pankhope nkumasekerera; komabe ululu ndi chisoni zitazikizira mozama m'mitima mwawo. Ha!, iwe mwana wa Mulungu, pali thandizo kwa mtima umene uli owawidwa. Mulungu akudikira kuti inuyo muthamangire kwa Iye ndi mtima wanu wosweka ndipo Iye adzakufungatirani ndi manja ake aakulu ndi achithonhozo amene ali achikondi komanso achisamaliro. Iye ndiye “thandizo lopezekeratu m'masautso.” Mulungu sadzachedwa, ndipo Iye adzakhalapo kuti akuthandizeni ndi kukupatsani chisamaliro pa china chilichonse chimene chimabweretsa nkhwana, kudandaula kapena chisoni.

Mneneri Yesaya ananenapo za zenizeni zokhudza chitetezo ndi chithandizo cha Mulungu: “Chifukwa Inu mwakhala linga la aumphawi, linga la osowa m'kuvutidwa kwake, pobisalira chimphepo, mthunzi wa pa dzuwa” (Yesaya 25:4). Anamondwe a moyo uno amene amavunduka koopsa ndipo amafuna kugonjetsa moyo wanu, pali kothawirako kwa Mpulumutsi wathu amene amasalira. Iwe mwana amene watopa, siuli wekha. Yesu Khristu amagwidwa ndi chifundo kwa iwo amene akuvutika ndi zinthu zosautsa zomwe mukukumana nazo lero, ndipo Iye analonjeza kuti adzakhala nanu. Pa Yesaya 43:1-3 timawerenga kuti: “Koma tsopano atero Yehova, amene anakulenga iwe Yakobo, ndi Iye amene anakupanga iwe Israele, Usaope, chifukwa ndakuombola iwe, ndakutchula dzina lako, iwe uli wanga. Pamene udutsa pamadzi ndili pamodzi ndi iwe; ndi pooloka mitsinje sidzakukokolola; pakupyola pamoto sudzapsa; ngakhale lawi silidzakutentha. Chifukwa kuti Ine ndine Yehova Mulungu wako, Woyera wa Israele,

(Yapitirira pa tsamba 2)



“Iwe mwana amene watopa, siuli wekha. Yesu Khristu amagwidwa ndi chifundo kwa iwo amene akuvutika ndi zinthu zosautsa zomwe mukukumana nazo lero, ndipo Iye analonjeza kuti adzakhala nanu.”

Mau a Mkonzi
3
Malonjezano a
Mulungu
4-5

Mu nthawi za nsautso
5
Tsekani khomo la
mtima wanu ku
kukaika 6

Kuyang'anizana ndi
dzuwa lam'mawa
Kuimba mu nthawi
ya nsautso
6

Nkhani zosiyanasiyana
7

Kodi Mukudziwa?
Mau a Nyengo Yake
8

ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA ZA...

Mau a Mulungu

2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

Ubale wa Chikondi

Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

Kulapa

Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

Kubadwa mwatsopano

Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;
Aef. 2:1, 5-6

Kupulumuka ku uchimo

1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

Chidzalo cha Mzimu Woyera

Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

Chiyero

Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16;
Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

Ufumu wa Mulungu

Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

Mpingo

Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13;
Akol. 1:18

Umodzi

Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

Maskaramenti

Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;
1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

Machiritso

Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

Chiyero cha Banja

Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;
1 Akor. 7:10-11

Chikhalidwe cha pakati pa anthu ena

1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

Masiku omaliza

2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;
Mat. 25:31-46

Kukhala mwa mtendere

Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

Kupembedza

Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

Kulalikira Uthenga Wabwino

Mrk. 16:15

(Kuchokera pa tsamba 1)

Mpulumutsi wako.” Lonjezolo silinali lakuti sipadzakhala mitsinje kapena moto, koma Mulungu akulonjeza kuti zimenezi sizidzawamiza ndipo kuti Iye adzakhala nafe.

Chifukwa chakuti Mulungu ndiye pothawirapo pathu ndi mphamvu yathu, Davide anapitirira kunena kuti, “Chifukwa chake sitidzachita mantha...” Ngakhale kuti anthu akhoza kukumana ndi mavuto a okhudza zauzimu, zandale, zathupi ndi zachuma, tikuyenera kuchita mantha, popeza kuti Mulungu ali mkatimo ndipo Iye adzathandiza anthu ake. Pa Masalimo 46:5 akunena kuti, “Mulungu adzauthandiza

“Mulole kuti mzimu
wanu umene wafooka
utsamire pa dzanja
lamphamvu la Yesu, ndipo
Iye adzakugwirizani
pamene mukuyenda mu
chipululuchi chimene
chili patsogolo panu.”

mbandakucha.” Mamasulidwe ena akunena mosangalatsa kuti, “dzuwa lisanatuluke.” Mu nthawi za mdima ndiponso usiku, Mulungu adzathandiza ndi kubweretsanso dzuwa lam’ mawa. Mwa Yesu Khristu, muli chiyembekezo kwa iwo osowa chiyembekezo, kulimbika kwa iwo amene mtima wao wafooka, ndipo machiritso kwa iwo amene asweka mtima.

Nthawi zambiri pamene mdima wafika pachimake usiku, zimaoneka ngati sikungayerenso,

koma pamenepo ndi pomwe kuunika kumayamba kuwala mu mdima umenewo. Ngati muli munkhondo ndipo mukuvutika, musaleme panjira. Mulole kuti mzimu wanu umene wafooka utsamire pa dzanja lamphamvu la Yesu, ndipo Iye adzakugwirizani pamene mukuyenda mu chipululuchi chimene chili patsogolo panu. Ngati mutadikira pa Ambuye, chipululu chanu chidzasanduka kasupe, ndipo mdima wanu udzasanduka kuwala kwa dzuwa.

Pamene maganizo anu achita nkhangungu ndi kusokonekera ndipo mzimu wanu sukuona kuti mutulukira kuti mu mavuto anu, “Khalani chete ndipo dziwani kuti Ine ndine Mulungu” (Masalimo 46:10). Zonse ndi zotheka ndi Mulungu, ndipo Iye sadzawasiya iwo amene aika chikhulupiriro chawo mwa Iye.

Moyo wochuluka ndiye zoonza zake za moyo wachikhristu, komabe izizi sizitichotsa ku nkhangungu zamkati ndi zakunja zomwe zili m’dziko ili lodzaza ndi mavuto. Nkhani yabwino ndiyo yakuti pali thandizo kumene tikhoza kuthawirako. “Mtima phee tisowa tonse, Zitivuta chabeko, Kaamba sitimanka konse, Kumpemphera Mlunguyo” (Bwenzi lathu ndiye Yesu). —Bro. Michael Smith

MUKHOZA KUPEZA MABUKU AMENE ATCHULIDWA MU KALATAYU MUTAPITA PA

www.churchofgodeveninglight.org

RAYS OF HOPE

THE SECRET OF THE SINGING HEART

HEART TALKS

Gospel Truth ndi kalata imene imasindikizidwa miyezi itatu iliyonse ndi a mpingo wa Church of God pofuna kulangiza ndi kulimbikitsa kuchokera mu zoonadi zopezeka mu Baibulo. Kutu mudziwe zambiri werengani pa intaneti popita pa www.thegospeltruth.org ndipo muvomere pa email imene mulandire ngati mukufuna kuti mudzilandira nawo kalatayi. Kalata ya *Gospel Truth* imasindikizidwa mu maiko ambiri kuti iperekedwe kwaulere m’dzikomo ndipo chuma chothandizira ntchitoyi chimachokera ku ndalama zimene ena amapereka mwaufulu. Ngati mukufuna lisiti yoonetsa zimene mwapereka, tidzakupatsani. —Editor, Michael Smith

Gospel Truth, P.O. Box 2042, Nixa, MO 65714 USA
editor@thegospeltruth.org

Mau a Mkonzi



Pakugwa ine ndidzaukanso; pokhala ine mundima Yehova adzakhala kuunika kwanga. —Mika 7:8

Yesu Khristu anabwera ku dziko lino lapansi chifukwa cha chikondi chachikulu cha Atate. Iye anamva kuwawa, anamva chisoni ndi masautso monga anthu amakumana nazo pofuna kuti izi zimuthandizire Iye kuti akhoza kumatipembedzera ife mwachifundo ndi motimvetsetsa. Mu nthawi imene mdima unali wochulukira, Yesu Khristu anabwera kudzadzutsa iwo akugwawo ndiponso kubweretsa kuunika kwa moyo umene unali mundima.

Munthu ataombedwa ku uchimo mwachisomo chopulumutsa cha Yesu Khristu, munthuyo akuyenera kukumamabe ndi nkhondo komanso mayesero a dziko lino. Mdani wa moyo wathu akuchita zonse zimene angathe pofuna kuti aononge chiyembekezo chathu ndikubweretsa nkhawa. Tikuyenera kugwiritsitsa kwathunthu pa malonjezo a Mulungu ndipo tikakamire pa mtanda, popeza pamene pali kuunika komanso moyo.

Mutu wathu ulendo uno ndi wakuti “Mu nthawi za mavuto.” Ngakhale kuti mwanjira ina iliyonse sitikufuna kumuyamikira mdaniyo kapenanso kupeputsa mtendere wodabwitsa umene umapezeka mwa Ambuye, tikuvomereza ndithu kuti moyo wathuwu umapitirira kukumana ndi mavuto pamene munthu wapulumutsidwa. Sitidzapulumutsidwa ku masautso a dziko lino mpaka pamene tidzafika kwathu kumwamba kumene tidzakhala kwamuyaya. Ndi mdalitso waukulu kukhala ndi Ambuye pambali yathu kuti ayende nafe ndi kutithandiza m’nthawi ya msautso.

Tikulalikira uthenga wa chigonjetso ndipo timaukhala mwa chisomo cha Mulungu. Komabe, pali ambiri amene atsala pang’ono kugonjetsedwa ndi mdima wa kukhumudwa ndi zopsinja zimene zimakhala kuchokera ku mbali zonse. Sindikufuna kupeputsa zoono zake za kulimbana kumene anthu opulumutsidwa akhoza kukhala nako mkati mwa miyoyo yawo pamodzi ndi zimene amakhudzidwa nazo ndi zoimvaimva za mthupi pamene ali pa ulendo wokhala ndi Mulungu.

Kalata uyu ndi wosiyana ndi makalata ena amene ndalemba mmbuyomu, ndipo ndi pemphero langa kuti akhala mdalitso komanso chilimbikitso kwa onse amene ali mnyengo za msautso. Kangapo konse, nanenso ndakhalapo m’ malo a mdima, ndipo pamene ndinapeza kuti kupezeka kwa chikondi cha Mulungu komanso chisamaliro chake zinabweretsa machiritso ku maganizo anga ndi mzimu wanga. Kothawirako kwa Mulungu ndi malo enieni, ndipo tikufunika kuti tikhale mu nthunzi wa chikondi cha Mulungu koposa kale.

Ana athu ndiponso achinyamata akukumana ndi zokhoma komanso zowapsinja zimene sizinaonekeko m’ mibadwo yapita. Mdaniyo alibe ulemu konse ndipo sasankha wakuti amuzunze. Iye akulimbana ndi oyera mtima a Mulungu powalipsira. Mphamvu ya Mulungu is yoposa mphamvu ya mdaniyo, ndipo ndi kuwala kwa Mulungu kokha kumene kungapangitse kuti mdimawo ukanganuke. Nthawi zambiri, anthu opulumutsidwa amachita manyazi kuvomereza zokhoma zimene akukumana nazo, ndipo nthawi zina sipakhala mwai kapena malo akuti akhoza kukamba momasuka za nkhondo zimene akukumana nazo. Ambuye ndiye ali ndi yankho lomaliza. Iye adzakhala “mphamvu yao m’nyengo ya nsautso” (Masalimo 37:39). Ndikufuna kulimbikitsa moyo uliwonse umene ukumva kupwetekedwa kuti upeze winawake wodalirika wakuti ukhoza kumuza nkhawa zako ndi kupemphera kuti mphamvu za mdima ziphanyike.

Mukukonedwa, simuli nokha ndipo Mulungu adzakhala wokhulupirika kwa inu!

Michael W. Smith

April 2021

“MISOZI INGACHEZERE KUGWA USIKU, M'MAŴA
KUMABWERA CHIMWEMWE CHOKHACHOKHA.”

MASALIMO 30:5



Mukafuna kutipeza

pa intaneti, mulembe

www.thegospeltruth.org

kuti mudzilandira makalata

athu kapenanso kuti

muone makalata akale.



Malonjezano a Mulungu

Chifukwa kuti pa tsiku la tsoka Iye adzandibisa mumsasa mwake, adzandibisa mkati mwa chihema chake; pathanthwe adzandikweza. —Masalimo 27:5

MULUNGU AMAKUKONDANI

Yehova anaonekera kwa ine kale, ndi kuti, Inde, ndakukonda iwe ndi chikondi chosatha; chifukwa chake ndakukoka iwe ndi kukukomera mtima. —Yeremiya 31:3



Adzatisiyanitsa ndani ndi chikondi cha Khristu? Nsautso kodi, kapena kupsinjika mtima, kapena kuzunza, kapena njala, kapena usiwa, kapena zoopsa kapena lupanga kodi? ... Koma m'zonsezi, ife tilakatu, mwa Iye amene anatikonda. Pakuti ndakopeka mtima

kuti ngakhale imfa, ngakhale moyo, ngakhale angelo, ngakhale maufumu, ngakhale zinthu zilipo, ngakhale zinthu zilinkudza, ngakhale zimphamvu, ngakhale utali, ngakhale kuya, ngakhale cholengedwa china chilichonse, sichingadzakhoze kutisiyanitsa ife ndi chikondi cha Mulungu, chimene chili mwa Khristu Yesu Ambuye wathu. —Aroma 8:35-39

MULUNGU ALI WACHIFUNDO

Chifukwa chakusathedwa ife ndicho chifundo cha Yehova, pakuti chisoni chake sichileka, chioneka chatsopano m'mawa ndi m'mawa; mukhulupirika ndithu. —Maliro 3:22-23

MULUNGU AMAMVA PEMPHERO

Munthu uyu wozunzika anafuula, ndipo Yehova anamumva, nampulumutsa m'masautso ake onse. —Masalimo 34:6

MULUNGU NDIYE POTHAWIRAPO

Ndipo Yehova adzakhala msanje kwa iye wokhalira mphanthi. Msanje m'nyengo za nsautso. —Masalimo 9:9

MULUNGU SADZAKUSIYANI

Khalani amphamvu, limbikani mitima, musamachita mantha, kapena kuopsedwa chifukwa cha iwowa; popeza Yehova ... Ndipo Yehova, Iye ndiye amene akutsogolera; Iye adzakhala ndi iwe, Iye sadzakusowa kapena kukusiya; usamachita mantha, usamatenga nkhawa. —Deuteronomo 31:6, 8

MULUNGU AMAPEREKA MTENDERE

Mtendere ndikusiyirani inu, mtendere wanga ndikupatsani; Ine sindikupatsani inu monga dziko lapansi lipatsa. Mtima wanu usavutike, kapena usachite mantha. —Yohane 14:27

MULUNGU ADZAKUTSOGOLERANI

Khulupirira Yehova ndi mtima wako wonse, osachirikizika pa luntha lako; umlemekeze m'njira zako zonse, ndipo Iye adzaongola mayendedwe ako. —Miyambo 3:5-6

MULUNGU AMATONTHOZA

Wolemekezeka Mulungu ndi Atate wa Ambuye wathu Yesu Khristu, Atate wa zifundo ndi Mulungu wa chitonhozo chonse, wotitonhoza ife m'nsautso yathu yonse, kuti tidzathe ife kutonhoza iwo okhala m'nsautso iliyonse, mwa chitonhozo chimene titonhozedwa nacho tokha ndi Mulungu. —2 Akorinto 1:3-4

MULUNGU AMAPEREKA MPUMULO

Idzani kuno kwa Ine nonsenu akulema ndi kuthodwa, ndipo Ine ndidzakupumulitsani inu. —Mateyu 11:28

Mu nthawi za nsautso

MULUNGU ADZAKONZANSO

Iye alimbisa olefuka, naonjezera mphamvu iye amene alibe mphamvu. Ngakhale anyamata adzalefuka ndi kulema ndi amisinkhu adzagwa ndithu: koma iwo amene alindira Yehova adzatenganso mphamvu; adzauluka pamwamba ndi mapiko monga ziombankhanga; adzathamanga koma osalema; adzayenda koma osalefuka. —Yesaya 40:29-31

MULUNGU ADZAPEREKA

Koma Mulungu wanga adzakwaniritsa chosowa chanu chilichonse monga mwa chuma chake mu ulemerero mwa Khristu Yesu. —Afilipi 4:19

MULUNGU ADZAPANGA NJIRA YOPULUMUKIRA

Sichinakugwerani inu chiyeso koma cha umunthu; koma Mulungu ali wokhulupirika, amene sadzalola inu kuyesedwa koposa kumene mukhoza; koma pamodzi ndi chiyeso adzaikanso populumukirapo, kuti mudzakhoze kupirirako. —1 Akorinto 10:13

MULUNGU ALI NDI MALINGALIRO PA INU

Pakuti ndidziwa malingiriro amene ndilingirira inu, ati Yehova, malingiriro a mtendere, si a choipa, akukupatsani inu adzukulu ndi chiyembekezero. —Yeremiya 29:11

MULUNGU ADZAKUMENYERANI NKHONDO

Ndipo Mose ananena ndi anthu, Musaope, chilimikani, ndipo penyani chipulumutso cha Yehova, chimene adzakuchitirani lero; pakuti Aejipto mwawaona lerowa, simudzawaonanso konse. Yehova adzakugwirirani nkhondo, ndipo inu mudzakhala chete. —Eksodo 14:13-14



MULUNGU NDIYE MTHANDIZI WANU

Kotero kuti tinena molimbika mtima, Mthandizi wanga ndiye Ambuye; sindidzaopa; adzandichitira chiyani munthu? —Ahebri 13:6

MULUNGU NDIYE MPHAMVU YANU

Ndikhoza zonse mwa Iye wondipatsa mphamvuyo. —Afilipi 4:13

YESERO LA CHIKHULUPIRIRO CHANU

M'menemo mukondwera, kungakhale tsopano kanthawi, ngati kuyenera, mukachitidwe chisoni ndi mayesero a mitundumitundu, kuti mayesedwe a chikhulupiriro chanu, ndiwo a mtengo wake woposa wa golide amene angotayika, ngakhale ayesedwa ndi moto, akapezedwe ochitira chiyamiko ndi ulemerero ndi ulemu pa vumbulutso la Yesu Khristu (1 Petro 1:6-7).

Ngati tiyenda chifupi ndi Mulungu, tidzapeza kuti mkati mwa mayesero athu, ngakhale ali owawa, pali chimwemwe chokoma chimene chimafalikira mpakana kutsikira ku miyoyo yathu. Chizindikiritso chakuti ife ndife ake a Ambuye, ndipo kuti amatikonda komanso kuti ndiye mthandizi wathu, chidzakhala chokoma mkati mwa masautso athu onse. Nthawi zina zimenezi zimatchingidwa ndi kukaikira kapena mantha a pa kanthawi; koma ngati

tibisala pansu pa mapiko ake ndiponso kumudalira iye kwathunthu, nsangalalo wa chimwemwe udzamveka m'mitima mwathu ngakhale tili mu nyengo zokhoma. Nthawi zina tikuyenera kumvetsera mosamalitsa, kuti timve mau ayeziyezi ndi okoma a nyimbo yake.

Khalani opirira m'mayesero anu; limbikani monga msilikali wabwino; sungani chishango cha chikhulupiriro: menyani nkhondo yabwino ya chikhulupiriro. Mu nthawi yake yoikika moyo wako udzaimba nyimbo za chigonjetso ndipo mabelu achimwemwe, ochokera mu kukoma kwa nyimbozo, adzaitana anthu a Mulungu kuti asangalale nanu limodzi mwa Ambuye ndi Mpulumutsi wanu.

—“Zonena za Mumtima” by C. W. Naylor

TSEKANI KHOMO LA MTIMA WANU KU KUKAIKA

“KUWALA KWA CHIYEMBEKEZO” BY D. O. TEASLEY



Kumukaikira Mulungu komanso mau ake ndi chizolowezi chimene chimabwera ndi mdzierekezi, ndipo chikawetedwa kwa nthawi, chimakula mphamvu ndipo sichiletseka. Kukaika kumapanga njira, kapena nseu mu bongo monga mmene imakhalira njira ya m'munda imene yayambika chifukwa mapazi ambiri adutsapo, ndipo

nkovuta kuti udzu umere. Chimodzimidzinsu, kukana kwathunthu komanso mphamvu ya Mulungu ndi zimene zikhoza kufufuta njira zimenezi zimenezi ndi kuphwanja chizolowezi cha kukaika. Ndibwerezanso kuti kukaika ndi chizolowezi, chimene chimabwera ndi mdzierekezi....

Ngati pali gawo loopsa la kukaika ndi pamene munthu akaikira zimene Mulungu wauchitira moyo. Iwo amene amangokhalira kukaika amapemphera kwambiri koma amakhulupirira pang'ono. Ngati Satana akhoza kukwanitsa kukupangitsani inu kuti mudzikaika zimene zinakuchitikirani ndipo simudzikhulupiriranso, akatero ndiye kuti wapeza polowera mu m'moyo wanu ndipo ngati simutseka mwansanga, akhoza kubweretsa mavuto ochuluka. Ndikudziwa anthu amene anakaika zimene Mulungu anawachitira, ndipo amapempha chikhululukiro kwa Mulungu, kenaka ndikumukaikiranso asamalize kupempherako. Mizimu yokaika ndi mizimu yongotsutsa imafanana ndi nthawi zambiri imagwirira ntchito limodzi.

Kwa anthu ena, kukaika ndi chikhalidwe chawo, ndipo kwaiwo nkosavuta kukaika kusiyana ndi kukukhulupirira. Ngati anthu otere atamachita ndi mizimu yokaikayo monga momwe anthu amachitira ndi anthu otsatsa malonda, sangamavutike kwambiri. Anthu otere samamulabadira wamalonda amene wabweretsa zinthu zake ngati iye akuwachonderera kuti amugule. Ngati anthu atamatseka khomo la mtima wao ku kukaika kulikonse ngakhale achondereredwe motani, zikatero posakhalitsa chikaikocho zikhocha osamabweranso kawirikawiri.

Zikaiko zili ngati alendo—ngati akusamalidwa bwino, amakhalitsa, koma ngati sakulabadiridwa ndipo mmalo mowasangalalira akupeputsidwa, sangakhalitse ndipo abwerera posachedwapa. Munthu wokaikayo amadziwa ndithu kuti chizolowezi chokaika chibweretsa chiwawa ndi kusautsika. ■


KUIMBA MU NTHAWI YA NSAUTSO

“CHINSINSI CHA MTIMA WOIMBA” BY C. W. NAYLOR



Moyo uli ndi mavuto ake. Ukuyenera kutero ndithu. Mavuto, ululu, zisoni ndiponso kukhumudwitsidwa zili ngati mphero pamene Mulungu amatisula ndi kutikonzanso. Zili ngati chitsulo chimene chimatipera ndi kutisalaza. Zilinsu ngati chitsulo china chimene chimatipangitsa kuti tiwale. Ngati sitingakhale wokondwa mpakana titafika pa nyengo yakuti palibe zonse zimene zikutipangitsa kuti tisakondwe zachotsedwa, tidzakhala ndi chimwemwe chochepa m'moyo uno. Popeza kukondwa sikuchokera ku kukhala m'moyo wa ntambasale kapena wongokhala. Kukondwa sikutanthauza kusowa kwa zokhoma ndi mavuto. Kukondwa kumachokera mu kugonjetsa mavutowo....

Mu nyengo ya mavuto timaimba nyimbo yosiyana ndi imene tingaimbe pamene zonse zili bwino. Tikuyenera kudzilimbitsa kuti tikhulupirire. Pamene tichita zimenezi, tikhoza kuimba nyimbo za chilimbikitso chimene chabwera popeza tikutsimikizika kuti Mulungu atithandiza. Tikhoza kuimba nyimbo za chikhulupiriro zimene zikhocha kupirikitsa mantha athu onse. Tikhoza kuimba nyimbo za chiyembekezo pamene tikuyang'ana moyembekezera za chigonjetso chimene chili patsogolo pathu komanso korona waulemerero amene tidzavale tikadzamaliza ulendowu. Tikhoza kuimba mwachimwemwe pokumbukira zisomo zimene Mulungu watonetsera m'mbuyomu. ■



KUYANG'ANIZANA NDI DZUWA LAM'MAWA

“CHINSINSI CHA MTIMA WOIMBA” BY C. W. NAYLOR



Nkwabwino kuyang'anizana ndi dzuwa pamene likutuluka. Ngakhale mu mdima, tikhoza kuyang'ana kummawa ndi chitsimikizo chakuti tsiku linanso kuwala kudzabwera.

Padzakhala abwenzi atsopano

mmalo mwa abwenzi akale amene anapita. Padzakhala chiyembekezo chatsopano pamene chiyembekezo china chatha, Padzakhala mwai watsopano pamene wakale wataika. Tiyeni tichotse maso athu kuchokera kumene dzuwa limalowera ndipo tiyang'ane kotulukira dzuwa podzikira tsiku latsopano komanso kuwala kwa ulemerero kumene kuunikirenso pa ife.

Tiyenera kuphunzira kuyang'ana dzuwa pomwe likutuluka. Chimene anthu ambiri amachita, mwachibadwidwe, ndiko kuyang'ana kumene dzuwa likulowera. Mkristu amene ali ndi chiyembekezo ndiye mkristu amene ali wachimwemwe. Iye amayang'ana kutsogolo kumene kuli zinthu zabwino. Iye sakhumudwa. Zinthu zabwino zonse sizikhala kumbuyo. Zinthu zimene zatayika zikhocha kubwezeretsedwanso. Chimene chili kutsogolo kwathu chimatengera mmene ife takonzekera kuti tikumane nalo tsogololo, zimene zili kunjira komanso chikhulupiriro chimene chimatipangitsa kuti tichilandire mwa njira yotani. ■

MULOLE CHIKHULUPIRIRO CHANU CHILAMULIRE MAMVEDWE ANU

“CHINSINSI CHA MTIMA WOIMBA” BY C. W. NAYLOR



Tikuyenera kukhala ndi chikhulupiriro pa moyo wathu wa chikhristu. Ndaona anthu ambiri okhumudwa ndi okaika. Nditawafunsa kuti, “Chavuta ndi chiyani?” ena anati, “Sindikupeza bwino.” Nditawafunsanso kuti, “Nchifukwa chiyani simukupeza

bwino?” ena anayankha kuti, “Sindikudziwa, komabe sindikupeza bwino.”

Mwinadi simukupeza bwino. Pamenepa ndiye titani? Mmene mukumvera m'maganizo anu si muyeso wa moyo wanu wauzimu. Anthu ena samva bwino m'thupi mwao pamene kenakake kochepe kavuta, ngakhale katakhala kuti sikoopsa. Enanso akhoza kumadzionetsa ngati ali bwino lomwe ngakhale pamene agwidwa ndi nthenda ina yoopsa. Nchimodzimodzinsu zauzimu. Ubale wanu ndi Mulungu sutengera mmene mukumvera m'maganizo anu. Zimene mumamva m'maganizo mwanu sizinayikidwe kuti zikhale muyeso wa chikhulupiriro chanu. Tikuyenera kuima m'chikhulupiriro, ndi kuphunzira kugwiritsa ntchito chikhulupiriro, komanso kuphunzira kukhala m'moyo wa chikhulupiriro. Mudziweruze nokha mwachilungamo. Musalole zimene mukumva m'maganizo anu zitsogolere chikhulupiriro chanu. China chakuti tikambepo nchakuti ngati mukhulupirira zabwino, mudzamvanso bwino, komabe nthawi zambiri chikhulupiriro chimakhazikika pa zimene munthu akumvaimva m'thupi m'malo mwa zenizenizo. Sizitengera kwambiri mmene mukumvera m'thupi mwanu. Kodi muli bwanji? Zimenezi ziyankhidwe ndi chikhulupiriro chanu, osati mmene mukumvera. Ndipo mukapeza yankholo, musalole kuti zimene mukumvaimvazo zikhalenso ngati mboni ya chikhulupirirocho.

Tikhazikitse chikhalidwe chakuti tsiku ndi tsiku tidzimanga moyo wathu ndi njerwa za chikhulupiriro, osati za chikaiko kapena mantha, nkhawa kapenanso zosamalira za moyo uno. Njerwa za chikhulupirirozi zilipo zambiri. Pamene tiphunzira kumanga ndi njerwa za chikhulupiriro, tiphunziranso chinsinsi cha mtima woimba — wa mkhristu amene ali wachimwemwe, wokondwa, komanso ali ndi chitsimikizo cha zakutsogolo, monga mmene ali ndi chitsimikizo cha zimene zilipo pano. ■

KULEPHERA KUMABWERETSA ZIGONJETSO ZAZIKULU

“CHINSINSI CHA MTIMA WOIMBA” BY C. W. NAYLOR



Kodi munayamba mwayeserapo kugonjetsa chinthu china chake kangapo konse komabe chikukusautsani? Tamverani, Paulo nayenso anakumana ndi zomwezo. Mwina mukukumbukira kuti kawirikawiri timamva za “munga m'thupi.” Paulo anayesetsa kuti auchotse. Koma Ambuye sanauchotse. Iwo anamuza kuti, “Chisomo changa chikukwanira.”

Nthawi zina timayesedwa kuti tidzione ngati ndife anthu olephera. Ndiganiza kuti tonsefe timalephera pa nthawi zambiri pa zimene tikuzikhumba komanso kuziyembekeza. Koma pali chinthu chimodzi chimene chili choona. Sitidzakhala olephera pokhapokha pamene tagonjera ku zimene zikuchitika pakati pathu komanso pamene taimika manja kuti sitipitiriza. Nthawi zinatatu, kuchokera ku kulephera ndi pamene pamabwera zigonjetso zazikulu.

Ngati simungakhale chimene inuyo mumakhumba mutakhala, komabe khalani chimene mungakwanitse, ndipo musachite manyazi ndi mmene muliri. Musalole kuti zimene mwalakwitsa kapena simunachite bwino zikulepheretseni kuchita chimene mukuyenera kuti muchite.

Mukhale bambo kapena mai amene mukhoza kuima njii ndi kuliyang'ana dziko pamodzi ndi zobetchera zake, kenaka monga mwamuna kapena mkazi lankhulani molimba mtima. Nenani, “Ndinalaphera inde, koma siine wokanika. Ndinalaphera inde, koma ndidzapambana.”

Pali zinthu zambiri zimene anthu amakumana nazo—mavuto a kunyumba, kusayenda bwino kwa bizinesi, ngongole, kulumala ndi matenda komanso zinthu zina zambiri. Komabe taonani anthu otchuka mu mbiri ya dziko, ndipo onani kuti naonso anali ndi mavuto ngati amenewo ndipo anawapambana napita chitsogolo.

Ngakhale kuti m'moyo wanu mukumane ndi nyengo yakuti simukudziwa kuti mutani, chonde musakhale pansu ndi kupindira manja kenaka nkumangolira. Yesetsani kupanga chinachake. Penapake pali njira ndithu yotulukira ndipo njira imeneyo idzakutsogolerani ku chigonjetso ndi chipambano. ■



“MOYO WANGA UKHALIRA CHETE MULUNGU YEKHA; CHIPULUMUTSO CHANGA CHIFUMA KWA IYE. IYE YEKHAYO NDIYE THANTHWE LANGA NDI CHIPULUMUTSO CHANGA; MSANJE WANGA, SINDIDZAGWEDEZEKA KWAKUKULU.” MASALIMO 62: 1-2



KODI MUKUDZIWA?

“Ziphona za Chikhulupiriro” za mu Chipangano Chakale zinadutsa mu zokhoma komanso mavuto ochuluka. Atumwi a mu Chipangano Chatsopano anakumana ndi owatsutsa ambiri ndipo onse anafa imfa zamazunzo kupatulapo mtumwi Yohane. Oyera mtima amene azungulira mpando wa Kumwamba anali iwo “akutuluka m’chisautso chachikulu” (Chivumbulutso 7:14). Masautso ndiponso mazunzo ndi gawo limodzi la moyo wa Mkhristu!



Mau a
Nyengo
Yake

KUZUNZIKA KUMABWERETSA MTIMA WOFUNA KUMVA CHISONI NDI ENA OVUTIKA

Kuti Mutipeze

The Gospel Truth
P. O. Box 2042
Nixa, MO 65714
USA

Email:
editor@thegospeltruth.org

“NKHANI ZA MUMTIMA” BY C. W. NAYLOR

Wolemekezeka Mulungu...wotitonthoza ife m’nsautso yathu yonse, kuti tidzathe ife kutonthoza iwo okhala m’nsautso iliyonse, mwa chitonthozo chimene titonthozedwa nacho tokha ndi Mulungu. —2 Akorinto 1:3-4

Ambuye atandiyitana ku ntchito yake, moyo wanga unalimbana ndi zinthu zazikulu. Mu zimenezo, ndinazunzika kwambiri. Nthawi zambiri ndinakhala kakasi, koma ndikayang’ana kumbuyo, ndimaona kuti zimenezo ndi zomwe zinandipangitsa kuti ndimvetsetse mtima wa munthu, komanso zinandipanga kukhala wokhudzidwa ndi mavuto a ena. Kuchokera nthawi imeneyo, zandithandiza kulowa mu zisoni ndi zosowa za anthu ena, kenaka nkuwatumikira powatonthoza ndiponso kuwathandiza kosiyana ndi mmene ndikadachitira. Kuzunzika kumene ndinazunzika poyambayamba kunatsekula zinsinsi zochuluka kwambiri ndiponso zinalemeretsa moyo wanga komanso ndi moyo wa ena. Pirirani zinthu izi modekha, popeza kudzera mu zimenezi inuyo mudzatuluka angwiro kuposa golide. Ngati simuzunzika, mukhala osapindulitsa kwambiri kwa iwo amene akuzunzika. Lonjezo ndi lakuti, “Ngati tizunzika naye, tidzachitanso ufumu ndi Iye.”



Abrahamu naye anazunzika mu nsembe imodzi yaikulu ija [ya mwana wake, Isake], koma chitsanzo cha kukhulupirika kwake mu yesero limeneli chimapindulitsa miyoyo yochuluka kwambiri. Yobu nayenso anazunzika osati kuthupi kokha, komanso ngakhale ku uzimu komwe anasautsika kwambiri, komabe kuzunzika kumeneko inali njira yokhayo yakuti Mulungu aonetsere chifundo chake ndi ubwino wake. Kodi popirira m’masiku a mdimawo, Yobu anaphunzira chiyani zokhudza Mulungu, nanga dzikoli laphunzirapo chiyani? Ngati tingachotsemo mu Baibulo nkhanu zimene zinalembedwa za mazunzo komanso zotsatira zake, ndiye kuti tichotsamo gawo limene liri labwino kwambiri ndiponso lopindulitsa. Tikhoza kukhala ausiwa ngati tingakhale ndi mbiri yopatulikayi imene ikhoza kumangonena za chimwemwe ndi mtendere ndiponso chitonthozo, komanso kumangokamba za chigonjetso ndi chipambano koma osanenako za njira yolimba imene tingayendemo kuti tikafike kumeneko! Ngati Ambuye watilanga, zimenezi zili ngati “phindu kwa ife;” ndipo pamene Mulungu watanthana, Iye akufuna kuti tichite bwino, choncho tikuyenera kudekha, ndiponso kupirira ngati tikumuona Iye amene ali Wosaonekayo. “Pirirani m’masautso,” imwani chikho cha Getsemane wanu, valani chisoti chaminga mosadandaula, ndipo pirirani mtanda wanu, popeza kwaperekedwa kwa inu kuti muzunzike naye ndiponso mulamulire pamodzi naye. ■

CHIYERO CHA KWA AMBUYE